# Maphunziro a m’Baibulo

Bible studies

## Petro

1. Mwamuna wopunduka waciritsidwa
2. Atumwi m’ndende
3. Hananiya ndi Safira anama kwa Ambuye
4. M’ndende mobwereza
5. Simoni wanyanga
6. Petro apita pa ulendo
7. Korneliyo
8. Petro m’nyumba ya Korneliyo
9. Petro m’ndende

Ndipo adzadza inu anthu onse cifukwa ca Dzina langa; koma iye wakupirira kufikira cimariziro, iyeyu adzapulumutsidwa. Mateyu 10.22

- Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com

# 1. Mwamuna wopunduka waciritsidwa

**Macitidwe a Atumwi 3.1-10 Wopunduka cibadwire aciritsidwa**

1. Koma Petro ndi Yohane analikukwera kunka ku Kacisi pa ora lakupembedza, ndilo lacisanu ndi cinai.
2. Ndipo munthu wina wopunduka miyendo cibadwire ananyamulidwa, amene akamuika masiku onse pa khomo la Kacisi lochedwa Lokongola, kuti apemphe zaulere kwa iwo akulowa m'Kacisi;
3. ameneyo, pakuna Petro ndi Yohane akuti alowe m'Kacisi anapempha alandire caulere.
4. Ndipo Petro, pompenyetsetsa iye pamodzi ndi Yohane, anati, Tiyang'ane ife.
5. Ndipo iye anabvombereza iwo, nalingirira kuti adzalandira kanthu.
6. Koma Petro anati, Silivia ndi golidi ndilibe; koma cimen ndiri naco, ici ndikupatsa, M'dzina la Yesu Kristu Mnazarayo, yenda.
7. Ndipo anamgwira iye ku dzanja lace lamanja, namnyamutsa; ndipo pomwepo mapazi ace ndi mfundo za kumapazi zinalimbikitsidwa.
8. Ndipo anazunzuka, naimirira, nayenda; ndipo analowa pamodzi nao m'Kacisi, nayenda, nalumpha, nayamika Mulungu.
9. Ndipo anthu onse anamuona iye, alikuyenda ndi kuyamika Mulungu;
10. namzindikira iye, kuti ndiye amene anakhala pa Khomo Lokongola la Kacisi: ndipo anadzazidwa ndi kudabwa ndi kuzizwa pa ici cidamgwera.

**Mafunso**

1. Kodi munthu wopunduka anali kukhala kuti? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi Petro ndi Yohane anapatsa ndalama kwa munthuyo wopunduka? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Petro ananena ciani kulingana ndi m'ndime 6?
4. Kodi ndi ciani cinacitika kwa munthu wopunduka? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi ndi yani amene anaciza munthuyo wopunduka?
6. Kodi munthuyo anacita ciani pambuyo pa kuciritsidwa? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Anthu anamuona munthuyo kuyenda ndi kuyamika Mulungu. Ndipo anadzazidwa ndi kudabwa ndi kuzizwa. Kodi mumadzazidwa ndi kudabwa ndi kuzizwa cifukwa Mulungu wathu wamphamvu?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao.

| 13 | 25 | 9 | 13 | 2 | 9 | 18 | 5 | 14 | 9 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | |

| 25 | 5 | 8 | 15 | 22 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 9 | 14 | 21 |
|---|---|---|
| | | |

| 4 | 26 | 9 | 11 | 15 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| 12 | 15 | 14 | 19 | 5 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| 12 | 1 |
|---|---|
| | |

| 16 | 1 | 14 | 19 | 9 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |

| 14 | 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| N | O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |

## 2. Atumwi m'ndende

**Macitidwe a Atumwi 4.1-22 – Petro ndi Yohane ku bwalo la akuru**

1 Koma m'mene analikulankhula ndi anthu, ansembe ndi mdindo wa ku Kacisi ndi Asaduki anadzako,
2 obvutika mtima cifukwa anaphunzitsa anthuwo, nalalikira mwa Yesu kuuka kwa akufa.
3 Ndipo anawathira manja, nawaika m'ndende kufikira m'mawa; pakuti mpa madzulo pamenepo.
4 Koma ambiri a iwo amene adamva mau anakhulupira; ndipo ciwerengero ca amuna cinali ngati zikwi zisanu.
5 Koma panali m'mawa mwace, anasonkhana pamodzi m'Yerusalemu oweruza, ndi akulu, ndi alembi;
6 ndi Anasi mkulu wa ansembe, ndi Kayafa, ndi Yohane, ndi Alesandro, ndi onse amene anali a pfuko la mkulu waansembe.
7 Ndipo m'mene anawaimika pakati, anafunsa kuti, Ndi mphamvu yanji, kapena m'dzina lanji, mwacita ici inu?
8 Pamenepo Petro, wodzala ndi Mzimu Woyera anati kwa iwo, Oweruza a anthu inu, ndi akulu,
9 ngati ife lero tiweruzidwa cifukwa ca nchito yabwino ya pa munthu wodwala, ndi maciritsidwe ace,
10 zindikirani inu nonse, ndi anthu onse a Israyeli, kuti m'dzina la Yesu Kristu Mnazarayo, amene inu munampacika pamtanda, amene Mulungu anamuukitsa kwa akufa, mwa Iyeyu munthuyu aimirirapo pamaso panu, wamoyo.
11 Iye ndiye mwalawo woyesedwa wopanda pace ndi inu omanga nyumba, umene unayesedwa mutu wa pangondya.
12 Ndipo palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwanalo.
13 Koma pakuona kulimbika mtima kwa Petro ndi Yohane, ndipo pozindikira kuti ndiwo anthu osaphunzira ndi opulukira, anazizwa ndipo anawazindikira, kuti adakhala pamodzi ndi Yesu.
14 Ndipotu pakuona munthu wociritsidwayoalikuimirira pamodzi nao, analibe kanthu kakunena kotsutsa.
15 Koma pamene anawalamulira iwo acoke m'bwalo la akulu, ananena wina ndi mnzace,
16 kuti, Tidzawacitira ciani anthu awa? pakutitu caoneka kwa onse akukhala m'Yerusalemu kuti cizindikilo cozindikirika cacitidwa ndi iwo, ndipo sitingathe kukana.
17 Komatu tiwaopse asalankhulenso m'dzina ili kwa munthu ali yense, kuti cisabukenso kwa anthu.
18 Ndipo anawaitana, nawalamulira kuti asanene konse kapena kuphunzitsa m'dzina la Yesu.
19 Koma Petro ndi Yohane anayankha nati kwa iwo, Weruzani, ngati nkwabwino pamaso pa Mulungu kumvera inu koposa Mulungu;
20 pakuti sitingatheife kuleka kulankhula zimene tinaziona ndi kuzimva.
21 Koma m'mene anawaopsanso anawamasula, osapeza kanthu kakuwalanga, cifukwa ca anthu; pakuti onse analemekeza Mulungu cifukwa ca comwe cidacitika.
22 Pakuti anali wa zaka zace zoposa makumi anai munthuyo, amene cizindikilo ici cakumciritsa cidacitidwa kwa iye.

**Mafunso**

1.Kodi ndi yani amene anaika Petro ndi Yohane m'ndende? Cifukwa ciani anacita tero? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Werengani ndime ya 4. Kodi anthu angati anakhulupirira?
3. Kodi mumakhulupirira Mau a Mulungu (Baibulo)?
4. Werengani ndime ya 12. Kodi ndi yani amene akhoza kutipulumutsa?
5. Ansembe ndi mdindo wa ku Kacisi ndi Asaduki sanalole Petro ndi Yohane kuphunzitsa m'dzina la Yesu. Kodi Petro ndi Yohane anamvera zimene iwo adauzidwa?
6. Kodi tingauze anthu ena za Yesu Kristu Mpulumutsi m'njira zotani?

## 3. Hananiya ndi Safira anama kwa Ambuye

**Macitidwe a Atumwi 5.1-11 – Za Hananiya ndi Safira**
1Koma munthu wina dzina lace Hananiya pamodzi ndi Safira mkazi wace,
2anagulitsa cao, napatula pa mtengo wace, mkazi yemwe anadziwa, natenga cotsala, naciika pa mapazi a atumwi.
3Koma Petro anati, Hananiya, Satana anadzaza mtima wako cifukwa ninji kudzanyenga Mzimu Woyera, ndi kupatula pa mtengo wace wa mundawo?
4Pamene unali nao, sunali wako kodi? ndipo pamene unaugulitsa sunali m'manja mwako kodi? bwanji cinalowa ici mumtima mwako? sunanyenga anthu, komatu Mulungu.
5Koma Hananiya pakumva mau awa anagwa pansi namwalira: ndipo mantha akuru anagwera onse akumvawo.
6Ndipo ananyamuka anyamata, namkulunga, namnyamula, naturuka naye, namuika.
7Koma atapita monga maora atatu, ndipo mkazi wace, wosadziwa cidacitikaco, analowa.
8Ndipo Petro ananena naye, Undiuze, ngati munagulitsa mundawo pa mtengo wakuti. Ndipo ananena, Inde, wakuti.
9Koma Petro anati kwa iye, Munapangana pamodzi bwanji kuyesa Mzimu wa Ambuye? Taona, mapazi ao a iwo amene anaika mwamuna wako ali pakhomo, ndipo adzakunyamula kuturuka nawe.
10Ndipo anagwa pansi pomwepo pa mapazi ace, namwalira; ndipo analowa anyamatawo, nampeza iye wafa, ndipo anamnyamula kuturuka naye, namuika kwa mwamuna wace.
11Ndipo anadza mantha akuru pa Mpingo wonse, ndi pa onse akumvaizi.

**Mafunso**
1. Chulani maina a mwamuna ndi mkazi wake amene anagulitsa munda wao. Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Hananiya ananamizira kuti anapatsa mtengo wonse wa munda wao. Kodi Petro anadziwa kuti sizinali ndalama zonse? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Petro ananena, ‘Sunanyenga anthu, komatu Mulungu’. Mulungu adziwa zonse. Kodi m’umoyo wanu muli mabodza?
4. M’1 Samueli 16.7 tiwerenga, ‘Munthu ayang’ana cooneka ndi maso koma Yehova ayang’ana mumtima’. Kodi ndime iyi itanthauzanji?
5. Ndi ciani cimene cinacitika ndi Hananiya? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
6. Ndi ciani cimene cinacitika pamene mkazi wa Hananiya anabwera kwa Petro? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi tingaphunzire ciani m’nthano iyi?

### Sewero
Lembani malembo pa malo ao (Numeri 23.19).

| 13 | 21 | 12 | 21 | 14 | 7 | 21 |
|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | |

| 19 | 9 | 14 | 4 | 9 | 25 | 5 | | 13 | 21 | 14 | 20 | 8 | 21 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | | | |

| 11 | 21 | 20 | 9 | | 1 | 14 | 1 | 13 | 5 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | |

| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |

| 14 | 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| N | O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |

# 4. M'ndende mobwereza

**Macitidwe a Atumwi 5.17-42**

17.Koma anauka mkulu wa ansembe ndi onse amene anali naye, ndiwo a cipatuko ca Asaduki, nadukidwa.
18. nathira manja atumwi, nawaika m'ndende ya anthu wamba.
19.Koma mngelo wa Ambuye anasegula pakhomo pa ndende usiku, nawaturutsa, nati
20. Pitani, ndipo imirirani, nimulankhule m'Kacisi kwa anthu onse mau a Moyo umene.
21. Ndipo atamva ici, analowa m'Kacisi mbanda kuca, naphunzitsa. Koma anadza mkulu wa ansembe ndi iwo amene anali naye, nasonkhanitsa a bwalo la akuru, ndi akulu onse a ana a Israyeli, natuma kundende atengedwe ajawo.
22. Koma anyamata amene adafikako sanawapeza m'ndende, ndipo pobwera anafotokoza,
23. nanena, Nyumba yandende tinapeza citsekere, ndi alonda alikuimirira pamakomo; koma pamene tinatsegula sitinapezamo mmodzi yense.
24. Koma m'mene anamva mau awa mdindo wa Kacisi ndi ansembe akulu anathedwa nzeru ndi iwo aja, kuti ici cidzatani.
25. Ndipo anadza wina nawafotokozera, kuti, Taonani, amuna aja mudawaika m'ndende ali m'Kacisi, alikuimirira ndi kuphunzitsa anthu.
26. Pamenepo anacoka mdindo pamodzi ndi anyamata; nadza nao, koma osawagwiritsa, pakuti anaopa anthu, angaponyedwe miyala.
27. Ndipo m'mene adadza nao, anawaika pa bwalo la akuru. Ndipo anawafunsa mkuru wa ansembe,
28. nanena, Tidakulamulirani cilamulire, musaphunzitsa kuchula dzina ili; ndipo taonani, mwadzaza Yerusalemu ndi ciphunzitso canu, ndipo mufuna kutidzetsera ife mwazi wa munthu uja.
29. Ndipo anayankha Petro ndi atumwi, nati Tiyenera kumvera Mulungu koposa anthu.
30. Mulungu wa makolo athu anaukitsa Yesu, amene munamupha inu ndi kumpacika pamtengo.
31. Ameneyo Mulungu anamkweza ndi Dzanja lace lamanja, akhale Mtsogoleri ndi Mpulumutsi, kuti apatse kwa Israyeli kulapa, ndi cikhululukiro ca macimo.
32. Ndipo ife ndife mboni za zinthu izi; Mzimu Woyeranso, amene Mulungu anapatsa kwa iwo akumvera Iye.
33. Koma m'mene anamva iwo analaswa mtima, nafuna kuwapha.
34. Koma ananyamukapo wina pa bwalo la akuru, ndiye Mfarisi, dzina lace Gamaliyeli, mphunzitsi wa cilamulo, wocitidwa ulemu ndi anthu onse, nalamula kuti atumwiwo akhale kunja pang'ono.
35. Ndipo anati kwa iwo, Amuna inu a Israyeli, kadzicenjerani nokha za anthu awa, cimene muti muwacitire.
36. Pakuti asanafike masiku ano anauka Teuda, nanena kuti ali kanthu iye mwini; amene anthu anaphatikana naye, ciwerengero cao ngati mazana anai; ndiye anaphedwa; ndi onse amene anmvera iye anamwazika, napita pacabe.
37. Atapita ameneyo, anauka Yuda wa ku Galileya, masiku a kulembedwa, nakopa anthu amtsate. Iyeyunso anaonongeka, ndi onse amene anamvera iye anabalalitsidwa.
38. Ndipo tsopano ndinena ndi inu, Lekani anthu amenewa, nimuwalole akhale; pakuti ngati uphungu umene kapena nchito iyi icokera kwa anthu, idzapasuka;
39. Koma ngati icokera kwa Mulungu simungathe kuwapasula; kuti kapena mungapezeke otsutsana ndi Mulungu.
40. Ndipo anabvomberezana ndi iye; ndipo m'mene adaitana atumwi, anawakhule kuchula dzina la Yesu, ndipo anawamasula.
41. Pamenepo ndipo anapita kucokera ku bwalo la akuru, nakondwera kuti anayesedwa oyenera kunyozedwa cifukwa ca dzinalo.
42. Ndipo masiku onse, m'Kacisi ndi m'nyumba, sanaleka kuphunzitsa ndi kulalikira Kristu Yesu.

**Mafunso**


1. Ndi cifukwa ciani atumwi anaikidwa mu ndende? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi mngelo wa Ambuye anacita ciani usiku? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Werengani ndime 29. Kodi tingaphunzire ciani m'ndime iyi?
4. Kodi mumamvera Mulungu? Mumamvera m'njira zotani?
5. Kodi Gamaliyeli anali munthu wotani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi anapatsa cilangizo cotani ku bwalo la akuru? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi atumwi ananenapo ciani pa kunzuzidwa? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

# 5. Simoni wanyanga

**Macitidwe a Atumwi 8.9-25 – Simoni wanyanga**
9Koma panali munthu dzina lace Simoni amene adacita matsenga m'mudzimo kale, nadabwitsa anthu a Samariya, ndi
kunena kuti iye yekha ndiye munthu wamkuru;
10ameneyo anamsamalira onsewo, kuyambira wamng'ono kufikira wamkuru, ndi kunena, Uyu ndiye mphamvu ya
Mulungu, yonenedwa Yaikuru.
11Ndipo anamsamalira iye, popeza nthawi yaikuru adawadabwitsa iwo ndi matsenga ace.
12Koma pamene anakhulupirira Filipo wakulalikira Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ndi dzina la Yesu Kristu,
anabatizidwa, amuna ndi akazi.
13Ndipo Simoni mwini wace anakhulupiranso: ndipo m'mene anabatizidwa, anakhalira ndi Filipo; ndipo pakuona
zizindikilo ndi mphamvu zazikuru zirikucitika, anadabwa.
14Koma pamene atumwi a ku Yerusalemu anamva kuti Samariya adalandira mau a Mulungu, anawatumizira Petro ndi
Yohane; 15amenewo, m'mene adatsikirako, anawapempherera, kuti alandire Mzimu Woyera:
16pakuti kufikira pamenepo nkuti asanagwe pa wina mmodzi wa iwo; koma anangobatizidwa m'dzina la Ambuye Yesu.
17Pamenepo anaika manja pa iwo, ndipo analandira Mzimu Woyera.
18Koma pakuona Simoni kuti mwa kuika manja a atumwi anapatsidwa Mzimu Woyera, anawatengera ndalama,
19nanena, Ndipatseni inenso ulamuliro umene, kuti amene ali yense ndikaika manja pa iye, alandire Mzimu Woyera.
20Koma Petro anati kwa iye, Ndalama yako itayike nawe, cifukwa unalingirira kulandira mphatso ya Mulungu ndi
ndalama.
21Ulibe gawo kapena colandira ndi mau awa; pakuti mtima wako suli wolunjika pamaso pa Mulungu.
22Cifukwa cace lapa coipa cako ici, pemphera Ambuye, kuti kapena akukhululukire iwe colingirira ca mtima wako.
23Pakuti ndiona kuti wagwidwa ndi ndulu yowawa ndi nsinga ya cosalungama.
24Ndipo Simoni anayankha nati, Mundipempherere ine kwa Ambuye kuti zisandigwere izi mwanenazi.
25Pamenepo iwo, atatha kucita umboni ndi kulankhula mau a Ambuye, anabwera kunka ku Yerusalemu, nalalikira
Uthenga Wabwino ku midzi yambiri ya Asamariya.

**Mafunso**
1. Chulani dzina la munthu wanyanga. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Anthu a ku Samariya anaganiza kuti Simoni anali ndi mphamvu ya Mulungu (ndime ya 10). Kodi tingasiyanitse bwanji mphamvu ya Satana ndi ya Mulungu?
3. Ndi ciani cimene cinacitika pamene Petro ndi Yohane anafika ku Samariya? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi Simoni anawapempha ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Petro anamuyankha bwanji? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Nanga ife tingagule mphatso ya Mulungu?
7. Kodi Petro anafuna kuti Simoni anacita ciani kulingana ndi ndime ya 22?
8. Nanga inu mumacita ciani mutacita zoipa?

**Sewero**
Lembani mau onse pa malo ao kukapeza yankho.




ufumu
Petro
Filipo
ulibe
mphatso
ndalama

## 6. Petro apita pa ulendo

**Macitidwe a Atumwi 9.32-43 - Aciritsidwa Eneya; aukitsidwa Tabita**
32Koma kunali, pakupita Petro ponse ponse, anatsikiranso kwa oyera mtima akukhalaku Luda.
33Ndipo anapeza kumeneko munthu dzina lace Eneya, amene anagonera pamphasa zaka zisanu ndi zitatu; amene anagwidwa manjenje.
34Ndipo Petro anati kwa iye, Eneya, Yesu Kristu akuciritsa iwe; uka, yalula mphasa yako. Ndipo anauka pomwepo.
35Ndipo anamuona iye onse akukhala ku Luda ndi ku Sarona, natembenukira kwa Ambuye amenewa.
36Koma m'Yopa munali wophunzira dzina lace Tabita, ndilo kunena Dorika; mkazi ameneyo anadzala ndi nchito zabwino ndi zacifundo zimene anazicita.
37Ndipo kunali m'masiku awa, kuti anadwala iye, namwalira; ndipo atamsambitsa iye anamgoneka m'cipinda ca pamwamba.
38Ndipo popeza Luda ndi pafupi pa Yopa, m'mene anamva ophunzirawo kuti Petro anali pomwepo, anamtumizira anthu awiri, namdandaulira, Musacedwa mudze kwa ife.
39Ndipo Petro anayamuka, napita nao. M'mene anafikako, anapita naye ku cipinda ca pamwamba; ndipo amasiye onse anaimirirapo pali iye, nalira, namuonetsa maraya ndizobvala zimene Dorika adasoka, pamene anali nao pamodzi.
40Koma Petro anawaturutsa onse, nagwada pansi, napemphera; ndipo potembenukira kumtembo anati, Tabita, uka. Ndipo anatsegula maso ace; ndipo pakuona Petro, anakhala tsonga.
41Ndipo Petro anamgwira dzanja, namnyamutsa; ndipo m'mene adaitana oyera mtima ndi amasiye, anampereka iye wamoyo.
42Ndipo kudadziwika ku Yopa konse: ndipo ambiri anakhulupirira Ambuye.
43Ndipo kunali, kuti anakhala iye m'Yopa masiku ambiri ndi munthu Simoni wofufuta zikopa.

**Mafunso**
1. Chulani dzina la wodwala manjenje. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi Petro anamuuza ciani munthuyo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Eneya anaciritsidwa m'dzina la yani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Eneya sanaciritsidwe cifukwa ca mphamvu ya Petro koma cifukwa ca mphamvu ya Yesu. Kodi anthu amene anaona mphamvu ya Yesu anacita ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Chulani dzina la wophunzira amene anacita nchito zabwino ndi zacifundo. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Ndi ciani cimene cinacitika ndi Dolika? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi Petro anacita ciani atalowa m'cipinda ca pamwamba? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
8. Kodi Petro ananena ciani kwa Dolika? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
9. Kulingana ndi ndime ya 42 kunali anthu ambiri amene anakhulupirira Ambuye. Nanga inu mumaika mtima wanu pa Mulungu?

**Sewero**
Pezani mau onse.

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| P | E | T | R | O | E |
| I | Y | N | A | O | N |
| W | O | U | K | A | E |
| E | P | U | S | E | Y |
| T | A | B | I | T | A |
| M | P | H | A | S | A |

Eneya
Petro
Yopa
iwe
nao
Tabita
Yesu
uka
mphasa

# 7. Korneliyo

**Macitidwe a Atumwi 10.1-16 – Kenturiyo Korneliyo**
1Ndipo kunali munthu ku Kaisareya, dzina lace Korneliyo, kenturiyo wa gulu lochedwa la Italiya,
2ndiye munthu wopembedza, ndi wakuopa Mulungu ndi banja lace lonse, amene anapatsa anthu zacifundo zambiri, napemphera Mulungu kosaleka.
3Iye anapenya m'masomphenya poyera, mngelo wa Mulungu alinkudza kwa iye, ngati ora lacisanu ndi cinai la usana, nanena naye, Korneliyo.
4Ndipo pompenyetsetsa iye ndi kuopa, anati, Nciani, Mbuye? Ndipo anati kwa iye, Mapemphero ako ndi zacifundo zako zinakwera zikhala cikumbutso pamaso pa Mulungu.
5Ndipo tsopano tumiza amuna ku Yopa, aitane munthu Simoni, wochedwanso Petro;
6acerezedwa iye ndi wina Simoni wofufuta zikopa, nyumba yace iri m'mbali mwa nyanja.
7Ndipo m'mene atacoka mngelo amene adalankhula naye, anaitana anyamata ace awiri, ndi msilikari wopembedza, wa iwo amene amtumikira kosaleka;
8ndipo m'mene adawafotokozera zonse, anawatuma ku Yopa.
9Koma m'mawa mwace, pokhala paulendo pao iwowa, m'mene anayandikira mudzi, Petro anakwera pachindwi kukapemphera, ngati pa ora lacisanu ndi cimodzi; ndipo anagwidwa njala, nafuna kudya;
10koma m'mene analikumkonzera cakudya kudamgwera ngati kukomoka;
11ndipo anaona pathambo padatseguka, ndi cotengera cirinkutsika, conga ngati cinsaru cacikuru, cogwiridwa pa ngondya zace zinai, ndi kutsikira padziko pansi;
12m'menemo munali nyama za miyendo inai za mitundu yonse, ndi zokwawa za padziko ndi mbalame za m'mlengalenga.
13Ndipo anamdzera mau, Tauka, Petro; ipha, nudye.
14Koma Petro anati, Iaitu, Mbuye; pakuti sindinadya ine ndi kale lonse kanthu wamba ndi konyansa.
15Ndipo mau anamdzeranso nthawi yaciwiri, Cimene Mulungu anayeretsa, usaciyesa cinthu wamba.
16Ndipo cinacitika katatu ici; ndipo pomwepo cotengeraco cinatengedwa kunka kumwamba.

**Mafunso**
1. Chulani dzina la kenturiyo. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Korneliyo anali munthu wopembedza ndi wakuopa Mulungu. Kodi ici citanthauzanji?
3. Nanga inu ndinu munthu wopembedza ndi wakuopa Mulungu?
4. Fotokozani zimene Korneliyo anaona m'masomphenya. Ndi m'ndime ziti mwapeza yankho?
5. M'ndime ya 4 tawerenga kuti Mulungu anamva pemphero la Korneliyo. Kodi Mulungu amamvanso pemphero lathu?
6. Kodi Petro anali kucita ciani pamene anyamata awiri ndi msilikari wopembedza anali pa ulendo wao? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Fotokozani zimene Petro anaona. Ndi m'ndime ziti mwapeza yankho?
8. Kodi Petro anayankha bwanji pamene anamva mau kuti ayenera kudya? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

**Sewero**
Pezani mau onse

| | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| M | A | S | O | M | P | H | E | N | Y | A |
| U | B | O | Y | R | R | E | F | L | G | I |
| L | M | D | I | P | H | A | T | J | M | A |
| U | A | N | L | G | N | N | I | R | N | I |
| N | W | U | E | L | J | Y | O | M | O | t |
| G | S | F | N | P | R | P | U | P | S | U |
| U | V | I | R | L | E | G | N | M | F | G |
| H | H | C | O | N | U | D | Y | E | B | T |
| S | R | T | K | S | I | M | O | N | I | G |
| R | W | O | P | E | M | B | E | D | Z | A |

masomphenya
mngelo
Petro
nudye
wopembedza
ipha
iaitu
Simoni
cifundo
nyumba
Korneliyo
Mulungu
wamba

## 8. Petro m’nyumba ya Korneliyo

**Macitidwe 10.17-36 ndi 44-48 – Petro ayenda kwa kenturiyo Korneliyo**
17Ndipo pokayika-kayika Petro mwa yekha ndi kuti masomphenya adawaona akuti ciani, taonani, amuna aja otumidwa ndi Korneliyo, atafunsira nyumba ya Simoni, anaima pa cipata,
18ndipo anaitana nafunsa ngati Simoni, wochedwanso Petro, acerezedwako.
19Ndipo m'mene Petro analingirira za masomphenya, Mzimu ananena naye, Taona, amuna atatu akufuna iwe.
20Komatu tauka, nutsike, ndipo upite nao, wosakayika-kayika; pakuti ndawatuma ndine.
21Ndipo Petro anatsikira kwa anthuwo, nati, Taonani, ine ndine amene mumfuna; cifukwa cace mwadzera nciani?
22Ndipo anati, Korneliyo kenturiyoyo, munthu wolungama ndi wakuopa Mulungu, amene mtundu wonse wa Ayuda umcitira umboni, anacenjezedwa ndi mngelo woyera kuti atumize nakuitaneni mumuke ku nyumba yace, ndi kummvetsa mau anu.
23Pamenepo anawalowetsa nawacereza. Ndipo m'mawa mwace ananyamuka naturuka nao, ndi ena a abale a ku Yopa anamperekeza iye.
24Ndipo m'mawa mwace analowa m'Kaisareya, Koma Korneliyo analikudikira iwo, atasonkhanitsa abale ace ndi mabwenzi ace eni eni.
25Ndipo panali pakulowa Petro, Korneliyo anakomana naye, nagwa pa mapazi ace, namlambira.
26Koma Petro anamuutsa iye, nanena, Nyamuka; inenso ndine munthu. 27Ndipo pakukamba naye, analowa, napeza ambiri atasonkhana;
28ndipo anati kwa iwo, Mudziwa inu nokha kuti sikuloledwa kwa munthu Myuda adziphatike kapena kudza kwa munthu wa mtundu wina; koma Mulungu anandionetsera ine ndisanenere ali yense ali munthu wamba kapena wonyansa;
29cifukwa cacenso ndinadza wosakana, m'mene munatuma kundiitana. Pamenepo ndifunsa, mwandiitaniranji?
30Ndipo Korneliyo anati, Atapita masiku anai, kufikira monga ora ili, ndinalikupemphera m'nyumba yanga pa ora lacisanu ndi cinai; ndipo taonani, padaimirira pamaso panga munthu wobvala cobvala conyezimira,
31nati Korneliyo, lamveka pemphero lako, ndi zopereka zacifundo zako zakumbukika pamaso pa Mulungu.
32Cifukwa cace tumiza anthu ku Yopa, akaitane Simoni amene anenedwanso Petro; amene acerezedwa m'nyumba ya Simoni wofufuta zikopa, m'mbali mwa nyanja.
33Pamenepo ndinatumiza kwa inu osacedwa; ndipo mwacita bwino mwadza kuno, Cifukwa cace taonani tiri tonse pano pamaso pa Mulungu, kumva zonse Ambuye anakulamulirani.
34Ndipo Petro anatsegula pakamwa pace, nati: Zoona ndizinkidira kuti Mulungu alibe tsankhu;
35koma m'mitundu yonse, wakumuopa iye ndi wakucita cilungamo alandiridwa naye.
36Mau amene anatumiza kwa ana a Israyeli, akulalikira Uthenga Wabwino wa mtendere mwa Yesu Kristu (ndiye Ambuye wa onse)
44Petro ali cilankhulire, Mzimu Woyera anagwa pa onse akumva mauwo.
45Ndipo anadabwa okhulupirirawo akumdulidwe onse amene anadza ndi Petro, cifukwa pa amitundunso panathiridwa mphatso ya Mzimu Woyera.
46Pakuti anawamva iwo alikulankhula ndi malilime, ndi kumkuza Mulungu. Pamenepo Petro anayankha,
47Kodi pali munthu akhoza kuletsa madzi, kuti asabatizidwe awa, amene alandira Mzimu Woyera ngatinso ife?
48Ndipo analamulira iwo abatizidwe m'dzina la Yesu Kristu, Pamenepo anampempha iye atsotse masiku.

**Mafunso**

1. Ndi ciani cimene cinacitika pamene Petro anali kukayika-kayika pa zimene anaona m'masomphenya? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kulingana ndi ndime ya 22 Korneliyo anafuna kumvetsa mau a Petro. Nanga inu mumafuna kumvetsa mau a Mulungu?
3. Kodi Korneliyo anacita ciani pamene Petro anafika ku nyumba yake?  Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi Petro anamlola kumlambira?  Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Mulungu amatilola kulambira anthu ena?
6. Fotokozerani ndime za 34 ndi 35.
7. Kodi m'masiku ano Mulungu alandirabe anthu amene amuopa ndi akucita cilungamo?
8. Kodi kuopa Mulungu kutanthauzanji?
9. Ndi ciani cimene cinacitika pamene Petro anali kulalikira?  Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao.

**Macitidwe a Atumwi 10.34**

| 13 | 21 | 12 | 21 | 14 | 7 | 21 |
|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | |

| 1 | 12 | 9 | 2 | 5 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| 20 | 19 | 1 | 14 | 11 | 8 | 21 |
|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | |

| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |

| 14 | 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| N | O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |

# 9. Petro m'ndende

**Macitidwe a Atumwi 12 – Petro mu ndende**
1. Koma nyengo imeneyo Herode mfumu anathira manja ena a m'Eklesia kuwacitira zoipa.
2. Ndipo adapha ndi lupanga Yakobo mbale wa Yohane.
3. Ndipo pakuona kuti kudakondweretsa Ayuda, anaonjezapo nagwiranso Petro. Ndipo awo ndi masiku a mkate wopanda cotupitsa.
4. Ndipo m'mene adamgwira, anamuika m'ndende, nampereka kwa magulu anai a alonda, lonse anai anai, amdikire iye; ndipo anafuna kumturutsa kudza naye kwa anthu atapita Paskha.
5. Pamenepo ndipo Petro anasungika m'ndende; koma Eklesia anampempherera iye kwa Mulungu kosalekeza.
6. Ndipo pamene Herode anati amturutse, usiku womwewo Petro analikugona pakati pa asilikari awiri, womangidwa ndi maunyolo awiri; ndipo alonda akukhala pakhomo anadikira ndende.
7. Ndipo taonani, mnge lo wa Ambuye anaimirirapo, ndipo kuunika kunawala mokhalamo iye; ndipo anakhoma Petro m'nthiti, namuutsa iye, nanena, Tauka msanga. Ndipo maunyolo anagwa kucoka m'manja mwace.
8. Ndipo mngelo anati kwa iye, Dzimangire m'cuuno, numange nsapato zako. Nacita cotero. Ndipo ananena naye, Pfunda cobvala cako, nunditsate ine.
9. Ndipo anaturuka, namtsata; ndipo sanadziwa kuti ncoona cocitidwa ndi mngelo, koma anayesa kuti alikuona masomphenya.
10. Ndipo m'mene adapitirira podikira poyamba ndi paciwiri, anadza ku citseko cacitsulo cakuyang'ana kumudzi; cimene cidawatsegukira cokha; ndipo anaturuka, napitirira khwalala limodzi; ndipo pomwepo mngelo anamcokera.
11. Ndipo Petro atatsitsimuka, anati, Tsopano ndidziwa zoona, kuti Ambuye anatuma mngelo wace nandilanditsa ine m'dzanja la Herode, ndi ku cilingiriro conse ca anthu a Israyeli.
12. Ndipo m'mene adalingirirapo, anadza ku nyumba ya Mariya amace wa Yohane wonenedwanso Marko, pamenepo ambiri adasonkhana pamodzi, ndipo analikupemp hera.
13. Ndipo m'mene anagogoda pa citseko ca pakhomo, linadza kudzabvomera buthu, dzina lace Roda.
14. Ndipo pozindikira mau ace a Petro, cifukwa ca kukondwera
sanatsegula pakhomo, koma anathamanga nalowanso, nawauza kuti Petro alikuima pakhomo.
15. Koma anati kwa iye, Wamisala iwe. Ndipo analimbika ndi kunena kuti nkutero. Ndipo ananena, Ndiye mngelo wace.
16. Koma Petro anakhala cigogodere; ndipo m'mene adamtsegulira, anamuona iye, nadabwa.

**Mafunso**
1. Chulani dzina la mfumu amene anapha Yakobo naika Petro m'ndende. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi Eklesia (mpingo) anacita ciani pamene Petro anali m'ndende? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Nanga inu mumacita ciani mukabvutika?
4. Petro anagona m'ndende cifukwa sanaope. Ndi cifukwa ciani Petro sanaope kulingana ndi inu?
5. Kodi Petro anacoka bwanji m'ndende? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi ndi cotheka bwanji kuit asilikali sanaone Petro ndi mngelo?
7. Kodi Petro anapita kuti atamasulidwa m'ndende? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
8. Kodi Roda anacita ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
9. Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi?

**Sewero**

Lembani malembo onse pa malo ao (Salimo 28.7)

| 25 | 5 | 8 | 15 | 22 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 14 | 4 | 9 | 25 | 5 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| 13 | 16 | 8 | 1 | 13 | 22 | 21 |
|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | |

| 25 | 1 | 14 | 7 | 1 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| 14 | 4 | 9 |
|---|---|---|
| | | |

| 3 | 9 | 11 | 15 | 16 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 3 | 1 | 14 | 7 | 1 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

;

| 13 | 20 | 9 | 13 | 1 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| 23 | 1 | 14 | 7 | 1 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| 23 | 1 | 11 | 8 | 21 | 12 | 21 | 16 | 9 | 18 | 9 | 19 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | | |

| 14 | 4 | 9 | 16 | 15 |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |

| 9 | 25 | 5 |
|---|---|---|
| | | |

| 1 | 14 | 1 | 14 | 4 | 9 | 20 | 8 | 1 | 14 | 4 | 9 | 26 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | | | | |

| 1 | 2 | 3 | 4 | 5 | 6 | 7 | 8 | 9 | 10 | 11 | 12 | 13 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |

| 14 | 15 | 16 | 17 | 18 | 19 | 20 | 21 | 22 | 23 | 24 | 25 | 26 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| N | O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |

## Mau a pa mtima

Mateyu 24.9. Pamenepo adzakuperekani kunsautso, nadzakuphani; ndipo anthu a mitundo yonse adzadana nanu, chifukwa cha dzina langa.

Aroma 2.11 Pakuti Mulungu alibe tsankhu.

Salimo 96.3 Fotokozerani ulemerero wace mwa amitundu; Zodabwiza zace mwa mitundu yonse ya anthu

Deuteronomo 18.10 Asapezeke mwa inu munthu wakupitiriza mwana wace wamwamuna kapena mwana wace wamkazi ku moto wa ula, wosamalira mitambo, kapena wosamalira kulira kwa mbalame, kapena wanyanga.

1 Samueli 16.7 Munthu ayang'ana cooneka ndi maso koma Yehova ayang'ana mumtima.

Yohane 16.33 Zinthu izi ndalankhula ndi inu, kuti mwa Ine mukakhale nao mtendere. M'dziko lapansi mudzakhala naco cibvuto, koma limbikani mtima; ndalilaka dziko lapansi Ine.